

# Maphunziro Oyambilira a Baibulo a moyo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera komanso woyeretsedwa

# Maphunziro Oyambilira a Baibulo a moyo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera komanso woyeretsedwa

Copyright © 2022 Charles Shaver

Buku iri la *Maphunziro Oyambilira a Baibulo a Moyo Wodzazidwa ndi Mzimu Woyera komanso Woyeretsedwa* linakozedwa ndi Charles Shaver. Ndi lotetezedwa ndi malamulo a dziko lonse a ufulu wa kasindikizidwe. Mukhoza kutulutsa kwa ulere kuti mugwiritse ntchito panokha. Koma kugwiritsa ntchito kwina kuli konse kumafunikira chilolezo cha mlembi.

Ma vesi a Baibulo mu maphunziro awa ndi ochokera mu MAWU A MULUNGU MU CHICHEWA CHA LERO

# Kagwiritsidwe ntchito ka phunziro iri

Liri lonse mwa maphunziro otsatirawa liri ndi mafunso a maziko a kuzamitsa ubale wanu ndi Khristu. Werengani mafunso ndipo funani yankho la funso limenelo mu Baibulo lanu. Ngati likunena kuti Yohane 1:12, likutanthauza kuti Buku la Yohane chaputala 1, vesi 12. Mndandanda wa maina a Baibulo kumayambiliro kwa Baibulo lanu udzafotokoza nambala ya tsamba la buku liri lonse. Pezani yankho mu Baibulo, kenako lembani mmawu anu anu.

Baibulo linatanthauziridwa mmatanthauziridwe osiyanasiyana, ndipo manenedwe a mawu mu matanthauziridwe ali wonse a Baibulo ndi osiyaniranapo. Muyenera kuloweza vesi mu matanthauziridwe amene akuveka bwino kwa inu, ngati matanthauziridwe amene muli nawo ndi osiyana.

Muyenera kudula kapena kukopera vesi loloweza kuti zikuthandizeni koloweza. Muziyenda nalo, kapena matani pa kalilore. Cholinga ndi ndi chakuti mukhale nalo pafupi kuti nthawi zonse mukaliwona, mukhoza kuphunzira kuloweza vesi.

# Malangizo kwa m'phunzitsi

Zikomo chifukwa cha kuthandiza ophunzira kuti amalize ndime za maphunziro. Mwachidiwikire, inu ndi ophunzira muzikumana kamodzi pa sabata kuti mubwerenso kuwona maphunziro. Ngati kungatheke, sungani maphunziro ena kwa ophunzira kuti achite phunziro limodzi pa nthawi mu kukumana kwanu. Kuphunzitsa phunziro limodzi pa sabata zimathandizira kutsimikizira kuti ophunzira akuvetsetsa maphunziro ndipo sakuchulukidwa.

# Phunziro 1 la Baibulo

# Kodi Mzimu Woyera ndi ndani?

Mwangolandira Yesu ngati Mpulumutsi komanso Mbuye wanu, ndipo mukumutsatira tsiku ndi tsiku. Mukuphunzira kuwerenga Baibulo ndi kupemphera. Mukhoza kufuna kudziwa zambiri za Mzimu Woyera. Phunziro iri likuthandizani kudziwa kuti Mzimu Woyera ndi ndani komanso mmene adzagwilire ntchito m'moyo mwanu.

1. Ezekeiel ananeneratu za tsiku limene Mzimu wa Mulungu adzachite ntchito ya padera mwa anthu. Kodi Mzimu adzachita chiyani mwa inu? (Ezikiel 36:26-27)
2. Yesu anakumana ndi imfa ya pa mtanda. Izi zinatanthauza kuti adzasiya ophunzira ake mwa thupi (Yohane 14:1-4). Kodi ndi ndani amene adzabwere kudzatenga malo a Khristu? (Yohane 14:16-17)
3. Kodi ndi malire otani amene Yesu akupereka pa kalandiridwe ka Mzimu Woyera? (Yohane 14:17)
4. Kodi Mzimu Woyera akuchita chiyani pa Yohane 15:26?

   Kodi ophunzira a Khristu, pakuvomera, amafunika kuchita chiyani? (Yohane 15:27)
5. Kodi ndi ntchito iti ya padera imene Mzimu Woyera adzachite mdziko? (Yohane 16:8-11)

   Fotokozani za nthawi imene Mzimu Woyera anakutsutsani.
6. Ndi ntchito iti yapadera imene Mzimu Woyera adzachita pakati pa ophunzira? (Yohane 16:13-14)

   Fotokozani za nthawi imene Mzimu Woyera anakutsogolerani.
7. James Moffatt akumasulira Yohane 14:16, "adzakupatsani nkhoswe ina." Werengani liri lonse mwa ma vesi awa, ndipo fotokozerani mmene Mzimu Woyera amakuthandizirani.

   a. Aroma 8:26

   b. Machitidwe 1:8

   c. Machitidwe 4:31

   d. 2 Petro 1:21

   e. Aroma 8:16

   Fotokozerani za nthawi imene Mzimu Woyera anakuthandizani.
8. A Khristu onse owona lero lino ali ndi Mzimu Woyera, monga mwa Aroma 8:9b. Kodi ndi ubale ozama motani ndi Mulungu umene ukufunika? (Aefeso 3:16, 19)
9. Kodi ndi ndani amene anatengapo mbali pa kutsanulira kapena kupereka Mzimu Woyera kwa ophunzira oyamba? Machitidwe 2:32-33)
10. Kodi ndi liwu liti limene limagwiritsidwa ntchito pa kufotokozera Mulungu pa 1 Petro 1:15-16?

    Kodi moyo wakukhala woyera umawoneka motani?
11. Kodi ndi ntchito yotani imene Mzimu Woyera amachita pa kukupangani kukhala Woyera (woyeretsedwa, wosambitsidwa, wopatulidwa)? (1 Petro 1:2)
12. Aroma 8:9 Mzimu Woyera amatchedwa Mzimu wa Mulungu. Kodi ndi dzina liti lina limene Mzimu Woyera akupatsidwa apa?

Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani akutchulidwa motero?

13. Kutengera pa zimene mwaphunzira mu phunziro iri, kodi munganene kuti Mzimu Woyera ndi ndani?
14. Kodi ndi kuti kumene Mzimu wa Mulungu akufuna akhale kuti lero? (1 Akorinto 3:16)
15. Rees Howell, a Welsh layman (1879—1950), woyambitsa Koleji ya za maphunziro a Baibulo ku Wales, anali munthu wa pemphero. Ngakhale analandira Khristu ndi kubadwa mwa Mzimu, anachitira umboni za kukumana kozama ndi Mzimu Woyera:

    > Anati kwa ine, "monga Mpulumutsi anali ndi thupi, motero inenso ndimakhala mu kachisi woyeretsedwa wa okhulupirira. Ndine munthu. Ndine Mulungu, ndipo ndabwera kudzakupempha kuti upereke thupi lako kwa ine ndi ndigwire ntchito kudzera mwa ilo. Ndikufuna thupi likhale kachisi wanga (1Akorinto 6:19). … zinatanthauza kali konse ka khalidwe langa la uchimo kanayenera kupita pa mtanda, kuti abweretse moyo wake ndi khalidwe lake." (Norman Grubb, *Rees Howell, Intercessor,* Fort Washington, Pa.: Christian Literature Crusade, 1952)

16. Kodi uthenga weni weni mu umboni uwu ndi otani kwa inu?

    Mwakhala mukukhala ndi maganizo omaliza pa za Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi mthandizi. Akufuna akuthandizeni. Mzimu Woyera ndi Mzimu wa Khristu. Akufuna kukupangani kukhala ngati Yesu. Mzimu Woyera ndi Mulungu. Ali ndi kuthekera.

Baibulo maka maka Buku la Machitidwe, likuuzani zambiri za Mzimu Woyera ndi ntchito yake. Mudzafunikira kuwerenga chaputala chimodzi mu Machitidwe pa tsiku m'maphunziro awa. Phunziro liri lonse lidzakhala ndi mafunso a pa Machitidwe komanso mabuku ena a Baibulo.

Tsopano muli ndi chidziwitso chabwino cha kuti Mzimu Woyera ndi ndani. Komabepali zambiri zakuti mudziwe za zimene akufuna achite m'moyo mwanu. Kodi ndinu okonzeka kuphunzira zambiri?

## Vesi Loloweza

Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani Nkhoswe ina kuti izikhala nanu nthawi zonse. Nkhosweyo ndiye Mzimu wa choonadi. Dziko lapansi silingalandire Nkhosweyi chifukwa samuwona kapena kumudziwa. Koma inu mumamudziwa pakuti amakhala nanu ndipo adzakhala mwa inu. (Yohane 14:16-17)

# Phunziro 2 la Baibulo

# Mzimu Woyera m'moyo wa Mkhristu

Moyo wa chikhristu ndi otheka ngati munthu "anabadwa mwa Mzimu" (Yohane 3:5, 8). Mkhristu aliyense ali ndi Mzimu Woyera. Tiyeni tipitilize kuwona mphatso iyi yochokera kwa Mulungu.

1. Werengani Yohane 3:1-15.
    a. Kodi udindo wa Nikodemo pa chipembedzo unali otani? (Yohane 3:1-2)
    b. Kodi Yesu ananena kuti ndi choyenereza chaching'ono chotani chimene chili choyenereza mu ufumu wa Mulungu (ulamuliro wa Mulungu)? (Yohane3:3)
    c. Kodi "kubadwa mwa Mzimu" kukufaniziridwa ndi chiyani ndipo ndi chifukwa chiyani? (Yohane 3:8)
    d. Kodi muyenera kuchita chiyani kuti muwone kubadwa kwa uzimu uku? (Yohane 3:15 ndi 1:12)
    e. Kubadwa kwa tsopano kumatanthauza moyo watsopano. Kodi moyo wanu watsopano mwa Mzimu kwasintha moyo wanu motani mmadera awa?
        (1) Pa kuthekera kwanu kwa kukonda?
        (2) Pakumvera kwanu kwa kumvera Mulungu?
        (3) Pa ma ubale anu ndi ena?
        (4) Pa mawonedwe anu pa chimo?
2. Uthenga wa Yohane umafotokoza za kubadwa kwa Uzimu kapena kubadwa mwa tsopano. Mwafotokoza njira zimene Mulungu wakupangani kukhala watsopano. Pambuyo pake mu chipangano chakale, Yohane akulembanso 1 Yohane ndipo akufotokozera za njira zina zowonetsera moyo wanu watsopano mwa Khristu. Kodi ndi ziti?
    a. 1 Yohane 4:7-8
    b. 1 Yohane 2:3
    c. 1 Yohane 5:4-5 ndi 4:4
    d. 1 Yohane 4:13
    e. 1 Yohane 5:18
3. Kodi ndi ziti mwa njira izi zimene mukufunikira nazo thandizo?
    Kodi ndi ziti mwa njira izi zimene mukumva bwino?
4. Ngati mwachimwa, muyenera kuchita chiyani? (1 Yohane 2:1-2)
5. Kodi mungadziwe bwanji kuti ndinu mwana wa Mulungu? (Aroma 8:16)
    Kodi munawona motani izi m'moyo mwanu?
6. Kodi ndi machenjezo otani amene akupatsidwa a Mzimu Woyera pa Aefes 4:29-32?
    Kodi choonadi ichi chikukuthandizani motani kumvetsa za Mzimu Woyera?
7. Kodi njira ya Paulo ya kufotokozera za kubadwa kwa Mzimu pa Aefeso 2:5, 8-10?

8. Kodi ndi pemphero lotani limene Paulo akupemphelera a Khristu a kwa Aefeso?

   a. Pa Aefeso 3:16

   b. Aefeso 3:19

9. Kodi ndi chiyani chimene chamakulimbikitsani kukhulupirira pemphero iri kuti likhoza kuyankhidwa m'moyo mwanu? (Aefeso 3:20-21)

10. Petro anakana Khristu pa nthawi ya kupachikidwa. Yesu ataukitsidwa kwa akufa, akuyankhula ndi Petro (Yohane 21:15-22). Kodi ndi chiyani chimene chinachitika kwa Petro chimene chinamupatsa mphamvu kukhala mtsogoleri wa mpingo oyamba? (Machitidwe 1:8; 2:2-4; 4:8)

    Kodi ndi chizindikiro chotani chimene chinali mu ulariki wake? (Machitidwe 2:41)

    Kodi ndi zofuna zotani za mphamvu ya uzimu zimene mwakhala nazo?

11. Kodi ndi lonjezo lotani la Mzimu Woyera limene Petro anachita? (Machitidwe 2:38-39)

    Kodi ndi chiyani chimene chifunika kuchitika poyabilira? (Machitidwe 2:38)

12. Amene tinganene kuti "oyang'anira a mpingo" oyambilira anasankhidwa pa Machitidwe 6:3. Kodi ndi zoyenereza zotani zimene iwo amene anasankhidwa anali nazo?

13. Kodi mumadziwa motani kuti Khristu amakhala mwa inu? (1 Yohane 3:24)

14. Charles Colson, othandizira udindo wa Purezidenti wa ku America Richard Nixon, amene anali ndi mulandu wa madzi ndipo analandira chilango chopita kundende. Ali mkati mwa kukhala m'ndende, anayamba kutsatira Khristu ndi kukhala chiphona cha kusintha ndende. Colson anatsogozedwa kwa Khristu ndi Tom Phillips, Purezidenti wa bungwe la Raytheon. Phillips anachitira umboni kwa Colson:

    > Sindinaoneke kukhala ndi kanthu kofunikira. Zonse zinali zopanda tanthauzo. Zinthu zonse za kuthupi m'moyo ndi zopanda tanthauzo ngati munthu sanawone zimene ziri kunsi kwake. … usiku wina ndinali ku New York kukachita za ntchito ndipo ndinazindikira kuti Billy Graham anali ndi msonkhano pa bwalo la Madison Square … ndinapita—mwachiyembekezo, ndikuganiza—kuyembekezera kuti ndipeza mayankho ena. Zonse zimene Graham ananena usiku umenewo zinakonza zinthu zambiri mu moyo wanga. Ndinaona zimene zimaperewera, ubale ndi Yesu Khristu, pakuti ndinali ndisanamuitane m'moyo mwanga, moyo wanga unali usanatembenukire kwa Iye. Choncho ndinatero—mkati kati mwa msonkhano.
    >
    > Ndinapempha Khristu kubwera m'moyo mwanga, ndipo ndinamva kufika kwake mu moyo wanga. Ndinamva kupezeka ndi kukhala kwa Mzimu mwa ine.  Ndipo ndinatuluka kukayenda m'makhwalala a ku New York. Sindinakondepo New York ndi kale lonse, koma usiku umenewu kunali kokongola. Ndinayenda dera ndi dera. Zinthu zonse zinaoneka zosiyana kwa ine.  Kunali kukugwa mvula mwa pang'ono pang'ono ndipo magetsi a mu mzinda anapanga kuwala kwa golide. China chake chachitika kwa ine ndipo ndinachidziwa. (Charles Colson, *Born Again,* Tappan, N.J.: Fleming H. Revell, 1976.)

15. Kodi umboni uwu ukunena chiyani kwa inu?

Mzimu Woyera wa Mulungu amagwira ntchito mwa inu, kukupangitsani kuti mudziwe Khristu. Moyo watsopano wa Mzimu, kupezeka kwake, chitsimikizo komanso utsogoleri ndi zanu. Koma nthawi zina mavuto a uzimu amabwera, pa kusatengera zimene Mzimu Wayamba. Mudzavetsetsa zimene zikuchitka ngati muphunzira phunziro lotsatira.

# Vesi Loloweza

Iwo amene amamvera malamulo ake amakhala mwa Iye, ndipo Iye amakhala iwo. Ndipo mmenemu ndi momwe timadziwira kuti Iye akukhala mwa ife. Timadziwa mwa Mzimu Woyera amene anatipatsa. (1 Yohane 3:24)

# Phunziro 3 la Baibulo

# Mavuto ndi mayankho

Moyo wanu watsopano mwa Khristu ukhoza kuyenda bwino mwa kanthawi, koma mosakhalitsa zovuta zonse za chikhristu zimabwera pa njira, zinthu zimene zimakuyendetsani chitsogolo pa ulendo wanu wa chikhristu. Mmene munachitira ndi zotchinga zimenezi zidzakhala zofunikira pa kutsimikizira mayendedwe anu ndi Khristu

1. Kodi uzimu wa ophunzira a Khristu unali otani lisanafike tsiku la Pentekoste (kutsanulidwa ndi kudzaza kwa Mzimu Woyera)?

   a. Luka 10:20

   b. Yohane 17:14

2. Kodi ndi mavuto otani amene mukuona m'maganizidwe a ophunzira?

   a. Luka 9 :53-54

   b. Luka 22:24

3. Kodi ndi maganizidwe otani amene Yesu amayembekezera kwa ophunzira ake? (Luka 22:26)

4. Kodi Yesu akupemphelera chiyani kwa ophunzira ake (komanso ife) pamene akufika kumapeto kwa nthawi ya utumiki wa pansi pano? (Yohane 17:17-20)

5. Werengani Agalatiya 5:13 -26.

   a. Kodi ndi vuto kapena sautso lotani limene a Khristu a ku Agalatiya anakumana nalo? (Agalatiya 5:17)

   b. Kodi Mkhristu amakwaniritsa motani chiyembekezo cha Mulungu?

      (1) Kodi ndi chiyani chimene chimapanga chilamulo? (Agalatiya 5:14)

      (2) Kodi choyamba cha chipatso kapena chokolola chimene Mzimu amaonetsa ndi chiyani? (Agalatiya 5:22)

      (3) Kodi ubale wanu ndi chilamulo uli poti? (Agalatiya 5:18)

   c. Kodi ndi chiyani chimene chiyenera kuchitika ndi khalidwe la uchimo kapena khalidwe la thupi (Agalatiya 5:17), monga mwa 5:24?

   d. Kodi zikhoza kutanthauza chiyani ngati "khalidwe la uchimo" "likanapachikidwa" m'moyo mwanu?

6. Kodi umboni wa Paulo unali otani? (Agalatiya 2:19-20)

   Kodi ndi ndani anali ndi ulamuliro pa moyo wake?

7. Kodi chisinsi cha chigonjetso chosalekeza ndi chiyani? Agalatiya (Agalatiya 5:22)

   Kodi izi zingagwire ntchito motani m'moyo mwanu?

8. Kodi mulingo wa uzimu wa Atesalonika unali otani? (1 Atesalonika 1:4-10)

   Kodi vuto lawo linali chiyani? (1 Atesalonika 3:10 komanso 4:3)

   Tsopano, kodi Paulo akuwapemphelera chiyani? (1 Atesalonika 5:23-24)

9. Kodi Mulungu akufunsa chiyani kuchokera kwa A Khristu? (Ahebri 12:14)

10. Kodi kuseri kwa machitachita a uchimo kuli chiyani? (Aefeso 2:2-3)

    Kuti muthandizika motani pa nkhaniyi mukawerenganso mawu a pa Yakobo 4:8?

11. Werengani Aroma 6 mpaka 8.

    a. Kodi Khristu wapereka chiyani kwa inu? (Aroma 6:6)

    b. Nenani "malamulo" anayi amene Paulo anathana nawo pa Aroma 7:22-23.

    c. Kodi yankho la Paulo linali chiyani pa vuto lake kapena sautso? (Aroma 8:2)

12. Ngakhale kuti Mzimu Woyera adzakumasulani kuchoka ku "chilamulo cha uchimo komanso imfa" (Aroma 8:2), kodi amachita chiyani ndi zifooko zanu? (Aroma 8:26)

13. Kodi kulimbana kwa pa Aefeso 6:12-13 ndi kwa chiyani? Kodi kulimbanako kukusiyana motani ndi nkhondo ya Mzimu ndi ndi chikhalidwe chizikonda pa Agalatiya 5:17?

14. Kumbukirani maganizidwe a ophunzira pa Luka 9:53-54 ndi Luka 22:24 (funso 2)? Kodi umoyo wawo wa uzimu ena mwa ophunzirawa ndi wotani monga mwa Machitidwe 4:31? Kodi tsopano akuonetsa khalidwe lotani? (Machitidwe 4:32-35)

15. Sherwood Wirt anagwira ntchito ngati mkonzi wa *Magazine ya Decision* ya bungwe la Billy Graham. Ngakhale anali mtsogoleri wa Chikhristu, Wirt anavomereza kulimbana kwa m'mtima mwake—nafuna chithandizo cha umulungu.

    Tsiku liri lonse la moyo wanga chikumbutso chakale chimatha kubwereranso kuchokera ku namtindi wa zinthu zakale, kubweretsa ku malingaliro zinthu zochitika zosasangalatsa zimene zinaonekera.

    Mu kukhala kakasi ndimalingalira za moyo wabwino umene ndinamvapo ndipo unachitikirapo ena.

    "Khalani okhululukira wabwino." Vuto linali lakuti sindinali kuiwala.

    "Ikani zinthu pamodzi." Ndimayesera koma zinthu zimangovuta

    "Kwilirani zoipa." Ndimatero; koma pakudziwa pamene ndakwilira, ndimakakamira kukumbanso.

    "Tayani mu nyanja ya chikhululukiro." Sindinathe kupeza Nyanja imeneyo pa mapu ya dziko.

    Panali patapita zaka ndisanakhale m'mawu, pa ndekha, mkati mwa moyo wanga. Ndinatembenukira ku Baibulo kuti ndipeze thandizo. Mu kalata ya Paulo yopita kwa Aefeso ndinapeza vesi, "Chotsani kuzondana, ukali ndi kupsa mtima mwa inu" [onani 4:31].

    Ndi wina amene anali kuchita zimenezi; zinali zodzutsa msinkhu wanga.

    Pa Yesaya 61 ndimawerenga, "Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine… ndikatonthoze anthu osweka mtima, ndikalengeze kwa akapolo kuti alandire ufulu ndiponso kuti ndikamasule a m'ndende." Kodi tsopano chosungunulira mavuto ichi—mafuta a chimwemwe opatsidwa ndi Mzimu Woyera ndi chiyani? Chimwemwe ndi chimene ndinaoneka kuti ndinali nacho mwa kanthawi kochepa …

    Zikuoneka kwa ine kuti ndinali kuimilira pakati pa kasupe opereka madzi pakati-kati pa chipululu. Mkati mwake ndimatha kumva madzi akuyenda chapatali; koma sanathetse ludzu langa, ndipo sindinadziwe njira yofikira kumeneko.

Choncho ndinadikira pa Ambuye ndipo anatchera khutu lake kwa ine. Anamva kudandaula kwanga – osatinso kwa ena pa nthawi imeneyi ayi, koma kwa ine ndekha.

Mawu awa ndi osavuta kunene, ndipo Mulungu amadziwanso. Koma pamene ndinamuuza kuti ndikulephera udindo wanga (moyo wanga wa chikhristu); pamene ndinati umunthu wanga waonongeka ndipo ndaponyedwa mu ukapolo; pamene ndinamufunsa kuti andipachike, analora chiganizo changa ndi kukwaniritsa pempho langa.

Munthawi yake ndipo mokomera Iye anatumiza othetsa mavuto wa umulungu mu mtima wa kusawutidwawu. Zinali ngati chifundizi cha dzuwa kuchotsa mphepo mnyengo yakuzizira.

Sindikudziwa kuti chikondi chinabweramo motani, koma ndikudziwa kuti mkwiyo onse umene ndinasungira anthu—kuphatikizapo iwo amene anali oyandikana ndi ine— unachoka. Nkhanza—kuwawidwa mtima—kumva kukhala odedwa—zonse zimene munganene. Zonse zinachoka. Kuwuma. Zinapita. (Sherwood E. Wirt, *Afterglow,* Grand Rapids: Zondervan Publishing House, 1976.)

16. Kodi mukuyankhapo motani pa umboni uwu?

Tikabadwa mwa Mzimu, tiyenera kuzindikira chikhalidwe chathu cha uzimu. Baibulo limati chikhalidwe cha uchimo chikhoza kupachikidwa! Tikhoza kupeza “lamulo la uchimo likugwira ntchito mwa ine” (Aroma 7:23). “lamulo la Mzimu Woyera wa moyo” (8:2) lingatimasule!

## Vesi Loloweza

Amene ali ake a Khristu Yesu anapachika pa mtanda thupi lawo la uchimo pamodzi ndi zokhumba zawo ndi zolakalaka zawo. Popeza timakhala ndi moyo mwa Mzimu Woyera, tiyeni tiyende pamodzi ndi Mzimu Woyera (Agalatiya 5:24-25).

# Phunziro 4 la Baibulo

# Kudzazidwa ndi Mzimu — kuyeretsedwa kwa thunthu

Pamene mwapanga chisankho chopereka moyo wanu kwa thunthu kwa Mulungu ndipo mwapempha kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, mudzakhala ndi ubale ozama ndi Mulungu. kuthana ndi nkhondo ya mkati iyi ya moyo wanu (imene wina ananena kuti “nkhondo ya pa chiweniweni ya mkati”) pa kukondera kwa thunthu kwa ulamuliro wa Mzimu, ndi chimene Baibulo limati kuyeretsedwa kwa thunthu.

1. Kodi mneneri wa chipangano chakale Yeremiya akuti njira ya tsopano ya Mulungu yochitira ndi anthu mtsogolo?
2. Kodi ndi uthenga otani umene Filipo analalikira kwa Asamaria? (Machitidwe 8:4-8, maka vesi 5)

   Kodi atumwi ku Yerusalemu anachita chiyani pa kuyankhapo? (Machitidwe 8: 14-17)
3. Kodi Paulo anapempherera chiyani kwa akhristu a ku Aefeso? (Aefeso 3:16, 19)
4. Khristu analangiza ophunzira ake kufalitsa uthenga wake. Kodi anawauza kuti achite chiyani kuti akonzekere ntchito iyi? (Luka 24:48-49)

   Kodi anapitiriza kufotokoza motani zimene Atate analonjeza? (Machitidwe 1:4-5)

   Kodi Mzimu adzawachitira chiyani iwo? (Machitidwe 1:8)
5. Kodi ndi kusintha kotani kumene a Khristu a kwa Akorinto anawona mu miyoyo yawo? (1 Akorinto 6:9-11, makamaka v.11)

   Liwu lakuti “kuyeretsedwa” limafotokozera Akorinto pa vesi 11. Nthawi zambiri, ichi chimafotokozeredwa ngati “chiyambi cha kuyeretsedwa” kodi ndi chizindikiro chotani chimene chilipo chakuti Akorinto amafunikira ubale wozama komanso wa thunthu ndi Mulungu? (1 Akorinto 3:1-3)
6. Kodi Mulungu wakhala akukuitani motani mu ubale wozama ndi Iye?
7. Anthu ambiri a mu Chipangano Chatsopano anafotokozeredwa kukhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Petro pa Machitidwe 4:8. Saulo (amene pambuyo pake anakhala Paulo) pa Machitidwe 9:17 komanso 13:9. Komanso Barnaba pa Machitidwe 11:24. Kodi mungamufotokoze motani munthu amene wadzazidwa ndi Mzimu?
8. Pambali pa “kudzazidwa ndi Mzimu Woyera” komanso “kuyeretsedwa kwa thunthu,” ndi mawu ena otani amene amafotokozera mwathunthu moyo wa kudzipereka komanso moyo wosambitsidwa?

   a. Mateyu 5:8

   b. 1 Yohane 4:17-18

   c. Ahebri 4:9-11

   d. Ahebri 6:1

e. Aroma 6:18

f. Kodi ndi oti mwa ma vesi awa amene akuyankhula kwa inu mwa mphamvu ndipo ndi chifukwa chiyani?

9. Kodi kufunikira kodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi chiyani?

a. Machitidwe 4:31-32

b. Machitidwe 6:5, 8 ndi 7:55. 59-60

c. Aroma 15:13

10. Pa 1 Atesalonika 1:3-8, okhulupirira akuyamikiridwa.

a. Kodi chifuniro cha Mulungu pa iwo chinali chiyani? (1 Atesalonika 4:3, 7)

b. Kodi kukana kwa langizo iri kunatanthauza chiyani? (1 Atesalonika 4:8)

c. Kodi Paulo akuwapemphelera chiyani? 1 Atesalonika 4:8)

d. Kodi ndi ndani amene amachita ntchito ya kuyeretsa komanso ndi yokwanira motani? (1 Atesalonika 5:23)

e. Kodi Paulo akupempherera chiyani pamwamba pa kuyeretsa? 1 Atesalonika 5:23)

f. Kodi ndi kulimba mtima kotani kumene muyenera kukhala nako kuti Mulungu adzayankha pemphero la kuyeretsedwa kwa thunthu m'moyo wanu? (1 Atesalonika 5:24)

11. Werengani Aefeso 5: 15-21.

a. Kodi ndi malamulo otani amene akuperekedwa kwa A khristu apa?

b. Pamene akunena kuti "kudzazidwa" pa Aefeso 5:18, ndi mawu a mvekero wa lero, kutanthauza kuti kupitiriza kudzazidwa. Kodi izi zikutanthauza chiyani m'moyo mwanu?

c. Pamene mukufunafuna kudzazidwa kudzazidwa ndi Mzimu mopitiriza, kodi Mzimu amadzera motani mwa inu kupita kwa ena?

(1) Aefeso 5:19

(2) Aefeso 5:20

(3) Aefeso 5:21

12. Pamene Yesu ananena za kulandira Mzimu Woyera pa Luka 11:13, anapereka choyenereza chosavuta. Kodi ndi chiyani?

13. Oswald Chambers anamwalira mu 1917 adakali mu zaka za m'ma 40. Uku kudali kumaliza kwa utumiki wake. Koma buku lake la *My Utmost for his Highest* likadali buku lomwe likugulidwa kwambiri. Pamene anali mwana, Chambers analandira Khristu. Patapita zaka, nthawi imene akuphunzitsa pa Koleji ya Dunoon, anamva F.B. Meyer akuyankhula za Mzimu Woyera. Chambers anachitira umboni:

> Ndinalibe masomphenya a kumwamba kapena angelo, ndinalibe chilichonse. Ndinali owuma opanda kanthu monga kale. Opanda mphamvu kapena kuzindikira Mulungu, popanda umboni wa Mzimu Woyera. Kenako ndinafunsidwa kuyankhula pa msonkhano, ndipo miyoyo makumi anayi inabwera patsogolo. Kodi ndinayamika Mulungu? Ayi, ndinali ndi mantha ndi kuwasiira kwa ogwira ntchito, ndikupita kwa Mr. MacGregor (mzanga) ndikumuuza zimene zinachitika, ndipo anati: "Kodi sukukumbukira kuyankhala za Mzimu Woyera ngati mphatso pa mawu a Yesu, ndipo anati: 'Mudzalandira mphamvu…'? Iyi ndi mphamvu yochokera

kumwamba." Modzidzimutsa china chake chinachitika mwa ine, ndipo ndinawona kuti ndinakhala ndikufuna mphamvu mdzanja langa, kuti ndinene ichi, ndikhoza kunena kuti—onani zimene ndiri nazo pakuika zanga zonse pa guwa.

Mu zaka zinayi zapitazo zakhala zovuta, zaka zisanu zakhala zabwino. Ulemelero kwa Mulungu, kupweteka kwa dzenje lozama la mtima wa munthu ladzadzidwa mpaka kusefukira ndi chikondi cha Mulungu. Chikondi ndi chiyambi, chikondi ndi chikatikati ndipo chikondi ndi chimaliziro. Akabweramo, zonse zimene umawona ndi "Yesu yekha, Yesu nthawi zonse."

Mukadziwa zimene Mulungu wakuchitirani, mphamvu komanso unyinji wa uchimo wapita ndipo kuwala konyezimira, kumasulidwa kosaneneka kwa Khristu kwabwera, ndipo pamene mukuona abambo ndi amayi amene akhale mafumu ndi mafumukazi okhazikika mwa Mulungu pa zinthu—oh, mumayamba kumvetsetsa zimene mtumwi Paulo amatanthauza pamene ananena kuti anafuna wozuzidwa kuchokera kwa Khristu kuti anthu apulumutsidwe! ...

Ndi chifukwa chake ndimayankhula kwambiri za kusintha khalidwe: Mulungu anasintha langa; ndinali pomwepo pamene anachita ichi. (Raymond Edman, *They Found the Secret,* Grand Rapids: Zondervan Publishing House, 1980.)

14. Kodi kuvomera kwanu ndi kotani ku umboni uwu?

Chimwemwe! Mukhoza kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mukhoza kuyeretsedwa kwa thunthu. Mungadzazidwe motani ndi Mzimu ndilo phunziro lathu lotsatira.

## Vesi Loloweza

Musaledzere ndi vinyo, chifukwa adzawononga moyo wanu. M'malo mwake mudzazidwe ndi Mzimu Woyera (Aefeso 5:18).

# Phunziro 5 la Baibulo

# Mungadzadzidwe motani ndi Mzimu — kuyeretsedwa kwa thunthu

Tsopano pakuti mukuzindikira zimene malemba amaphunzitsa, mukhoza kukhala kuti mukufuna kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kuyeretsedwa kwa thunthu. Baibulo limafotokozera mmene izi zimachitikira.

1. Kodi ndi mchitidwe otani umene umakulorani kuti muyeretsedwe kapena kukupangani kukhala woyera?
   a. Ahebri 10:10-14
   b. Ahebri 13:12
2. Yohane 12:24-25 ndi chitsanzo cha moyo wa chikhristu. Kodi ndi zinthu ziti m'moyo mwanu zimene zifunika "kugwa pansi ndi kufa" ndi cholinga chakuti inumupezeke ku kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu?
3. Werengani 1 Yohane 1:7
   a. Kodi ndi chiyani chimene chimatisambitsa kapena kutiyeretsa?
   b. Kuchokera ku uchimo ochuluka motani?
   c. Kodi chonereza chofunikira pa kuyeretsedwa ndi chiyani?
   d. Kodi zikutanthauza chiyani kwa inu "yendani m'kuunika" kapena khalani m'kuunika?
4. Kodi ndi ndani amene ali woyenera kulandira chidzalo cha Mzimu ndi kuyeretsedwa kwa thunthu? (Machitidwe 5:32)
5. Kodi ndi mphatso yotani imene Yesu akuuza ophunzira kuti adikilire pa Machitidwe 1:4-5?
6. Kodi Yesu anawuza ophunzira ake chiyani za kupemphelera Mzimu Woyera? (Luka11:9-13)
7. Werengani Aroma 12:1-2. Kodi "abale awa" (a pa banja la Mulungu) akupemphedwa kuchita chiyani ndi matupi awo?

   Kodi zingatanthauze chiyani kwa inu "kupereka thupi lanu [kukhala] nsembe ya moyo … kwa Mulungu"?
8. Kuti ophunzira adzazidwe ndi Mzimu, kodi zikutenga nthawi yaitali bwanji?
   a. Machitidwe 2:4
   b. Machitidwe 8:15-17
9. Kodi ndi ndani amene amakuyeretsani? (1 Atesalonika 5:23)
10. Kodi mumalandira motani Mzimu mwathunthu kapena kukhala woyeretsedwa mwathunthu?
11. Ndipo patatha chaka chitembenukireni mtima Stanley Jones anakhala mu chimwemwe chachikulu. Kenako anapeza kuti mamvedwe oipa, kukwiya komanso kulimbana kwakukulu kunakula m'moyo mwake. Zochitika zambiri m'moyo zinali chipambano, koma panali zolowelera zosokoneza. Iye analemba:

Ndinali pa mavuto. Koma ndinatetezedwa ndi kulimbana kwa mkati. Ndipo khomo linatseguka mkatikati mwa kulimbana, linatseguka kudzera mu buku. Pamene ndinatenga buku limenelo mu nyumba ya mabuku, ya sande sukulu, ndinamva kufulumizidwa kwa kutumikira kudzera mwa ilo. Mtundu wa chithunzi chokhala ndi mbali zitatu chinabwera mwa ine. Chithunzi cha chiyembekezo. Ndinayamba kuwerenga chisinsi cha mkhristu cha moyo wokondwera (Christian's Secret of a Happy Life), lolembedwa ndi, Hannah Whitall Smith, bwezi la chipembedzo. Linanena za chigonjetso chonse cha munthu yense wa thunthu. Moyo wanga unayaka ndi chikhumbokhumbo pamene ndimawerenga. Sindimaliwerenga koma ndimalidya. Ndinapeza tsamba lowerenga kwa mphindi makumi anayi pamene Mulungu anayankhula kwa ine: "Tsopano ndi nthawi ya kupeza." … Ndinayesera kupitiriza kuwerenga, koma mawu sanawonekenso… Ndinatseka buku, ndikugwada pa mawondo pambali pa kama wanga, ndikunena kuti "Tsopano Ambuye kodi ndichite chiyani?" Ndipo anayankha: "Kodi udzandipatsa zako zonse?" Mochedwerapo ndinayankha: "Inde Ambuye, nditero, ndikupatsani zanga zonse, zonse zimene ndimazidziwa, ndi zina zonse zimene sindizidziwa." Ndipo anayankha "Tenga zanga zonse, tenga Mzimu Woyera." Ndinakhala chete mwa kanthawi: zanga zonse kukhala zake zonse, zanga zonse zinali ine mwini, zake zonse zinali Iye mwini, Mzimu Woyera." Ndinadzuka pa mawondo anga, popanda chizindikiro, ndinasunga mawu ake. Khalidwe lake linali kuseri kwa mawu amenewo. … Ndinayendayenda mu chipinda kubwereza kuvomera kwanga. Kukaikira kunayamba mwa ine. Ndinachita zimene Abrahamu anachita pamene mbalame zinabwera kudzamwaza nsembe yake—anaziyinga. Ndinayenda mu chipinda kumathamangitsa ndi manja kukaikira kwakulu kochititsa mantha. Ndi pamene mwadzidzi ndinadzadzidwa — ndinadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Mowonjezawonjeza kwa Mzimu kunawoneka kuti kukuyenda mwa ine ngati moto wonyeketsa. Ndimayenda pansi ndi misozi ya chimwemwe ikutsikira mu masaya mwanga. Sindikanachita chilichose koma kumuyamika— ndipo ndinachita. Ndinadziwa kuti awa simamvedwe odutsa; Mzimu Woyera wabwera kudzakhala ndi ine kwa nthawi zonse. (E. Stanley Jones, *A Song of Ascents*, Nashville: Abingdon Press, 1968)

Kodi kuyankha kwanu pa umboni uwu ndi kotani?

12. Muphunziro iri mukhoza kukhala kuti mwaona mitu ina ikuoneka mobwerezabwereza kwa iwo amene ayeretsedwa kapena kudzazidwa ndi Mzimu Woyera:

a. Zokhudza. Machitidwe 1:12-14 ndi Luka 11:9-10, 13 (funso 6)

b. Kusambitsa. 1 Yohane 1:7 (funso 3)

c. Kupatulidwa. Aroma 6:13 komanso Aroma 12:1-2 (funso 7-8)

d. Kulengeza. Machitidwe 26:18 komanso Agalatiya 3:14 (funso 11)

Lembani pemphero kupempha kudzaza kwa Mzimu Woyera m'moyo mwanu kapena pemphero la kuyamika chifukwa cha kukudzazani.

Kodi Mulungu wakuchitirani chiyani?

Yamikani Mulungu chifukwa cha zimene wakuchitiran!

Pamene mwadzazidwa ndi Mzimu (kapena kuyeretsedwa mwathunthu), ndikofunika kupitiriza ubale umenewo. Choncho Mkhristu ayenera kuyenda mwa Mzimu kapena kukhala mwa Mzimu. Ubale osangalatsa ndi wopitabe patsogolo wafotokozeredwa mu phunziro lotsatira.

## Vesi Loloweza

Mulungu mwini, Mulungu wa mtendere, akuyeretseni kotheratu. Mzimu wanu wonse, moyo ndi thupi zisungidwe zopanda cholakwa mpaka kubwera kwa Ambuye athu Yesu Khristu. Amene anakuitanani ndi wokhulupirika ndipo Iye adzachita zimenezi. (1 Atesalonika 5:23-24).

# Phunziro 6 la Baibulo

# Kuyenda mu Mzimu

Munthu akadzazidwa ndi Mzimu, moyo watsopano umayamba. Awa simathero, koma chiyambi cha chisangalalo, kudalira pa Mzimu kwa nthawi ndi nthawi. Agalatiya 5:25 amafotokozera za ichi ngati "kuyenda mosasiyana ndi Mzimu," komanso Aroma 8:4 amayankhula za iwo "amene sayenda monga mwa thupi koma monga mwa Mzimu."

1. Werengani Akolose 1:21-23.
   a. Kodi imfa ya Khristu inapereka chiyani kwa Akolose?
   b. Kodi Mulungu akanawapereka motani?
   c. Kodi akuyenera kuchita chiyani? (1:23)
2. Kodi Aroma 12:2 amatipempha kuchita chiyani mosalekeza?

   Kodi ndi njira zina ziti zimene mumasandulika nazo pakukozanso kwa maganizo anu?
3. Pa 1 Atesalonika 5:23, Paulo akupemphera kuti Mulungu apitirize kukuyeretsani nthawi ndi nthawi. Kodi zotsatira za nthawi yotalika ndi chiyani?

   Kodi ndi ndani amene amatetezera kapena kusamalira? (1 Atesalonika 5:24)

   Kodi ndi njira zina ziti zimene Mulungu amasunga anthu ake?
4. Kodi ndi mawu oti amene akugwirizana ndi ubale opitirira ndi Mzimu?
   a. Agalatiya 5:16-18
   b. Agalatiya 5:25

   Kodi ndi mawu oti amene ali ndi tanthauzo kwa inu, ndipo ndi chifukwa chiyani?
5. Werengani Aroma 8:1-4, 8-9.
   a. Kodi MzimuWoyera anachita chiyani kwa Paulo? (vesi 2, "kumasula" akuwonetsa kenakake kochitika mu ka nthawi kakang'ono)
   b. Kodi ndi chiyani chimene chiyenera kuchitika pa kukwaniritsa zoyenera za chilamuro mwa ife? (Aroma 8:4)
   c. Kodi ndi chiyani chimene chimakutetezerani kuti musalamuliridwe ndi chikhalidwe cha uchimo (kapena "thupi")? (Aroma 8:8-9)
   d. Kodi ndi zochitika liti za paderadera zimene zidzawonetsere khalidwe lanu ngati muli wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera?

      (1)

      (2)

      (3)
6. Kodi Mzimu Woyera angakuchitireninso chiyani pambuyo pa kukudzazani?

   a. Machitidwe 1:8

   b. Machitidwe 9:31

c. Machitidwe 13:4

d. Machitidwe 20:28

e. Aroma 8:14

f. Aroma 8:26

Kodi ndi chinthu chiti chimodzi chimene Mzimu Woyera wakuchitirani kuyambira nthawi imene anakudzazani?

7. kolinga ndi 1 Yohane 2:1-2, chimo silikuyenera kukhala mbali imodzi ya moyo wanu wa Chikhristu; koma ngati muchita chimo, muyenera kuchita chiyani?

   Kodi lonjezo la kupitiliza ku pitiriza kusambitsidwa limene liri pa 1 Yohane 1:7?

   Kodi zimatanthauza chiyani kwa inu kuyenda kapena kukhala mu Mzimu?

8. Pa Machitidwe 2:4 komanso Machitidwe 4:31 anthu akudzazidwa ndi Mzimu. Kodi ndi liti limene munafuna kapena munalandira kukhudza kwatsopano kwa Mzimu wa Mulungu?

9. Mutadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kuyeretsedwa nwa thunthu, muyenera kupitiriza ubale wanu ndi Mulungu pa kuyenda tsiku ndi tsiku mwa Mzimu. Ngati china chake chitalowelera mu ubale wathu ndi Mulungu, tifune kubwezeretsedwa (1 Yohane 2:1). Moyo wa Hudson Taylor, mtumwi wamkulu komanso oyambitsa utumwi ku dziko la China, ndi chitsanzo chabwino cha izi. Atakhala Mkhristu kumene ali ndi zaka17, anayeretsedwa. Patatha zaka ku utumwi, anali osakondwa komanso osamva bwino. Pakutha pa zaka analemba:

   > Musatilore kuti tisinthe mawu a Khristu. Si "ali yense amene wamwa" koma "aliyense amene amene adzamwa" [Yohane 4:14]. Si dontho limodzi lokha lopaturidwa, koma khalidwe lopitirira la moyo. Pa Yohane 6:35, pameneponso tanthauzo la thunthu ndi, "Iye amene abwera kwa ine sadzamva njala. Ndipo iye amene akhulupirira ine sadzamva ludzu." … zikuoneka kwa ine kuti pamene ambiri mwa ife timalakwitsa ndi kusiya kumwa kwathu mmbuyo, pamene ludzu lathu likupitilira kufikira lero. Chimene tikufunikira ndi kumamwa – inde, kuyamika chochitika chiri chonse chimene chimatipangitsa kuti tizimwa kwambiri madzi a moyo. (Howard Taylor, *Hudson Taylor's Spiritual Secret,* Chicago, Moody Bible Institute, no date)

   Kodi ndi phunziro lotani limene mwaphunzira kuchokera mu umboni uwu?

10. Kodi ndi zinthu ziti zitatu zofunikira kwa inu kuti muyende ndi Mzimu?

Mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu komanso woyenda mwa Mzimu ayenera kuzindikira malire amene Mzimu adzachita m'moyo uno. Pali zinthu zina zosungidwira kumwamba. Malire amenewo ali mu phunziro lotsatira.

# Vesi Loloweza

Ndi cholinga chakuti chilungamo chofunikira cha lamulo chikwaniritsidwe kwathunthu mwa ife amene sitikhala monga mwa chikhalidwe chathu cha uchimo koma mwa Mzimu (Aroma 8:4)

# Phunziro 7 la Baibulo

# Malire a mbali ino ya Kumwamba

Mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu ndipo akuyenda mwa Mzimu adzakondwerera chigonjetso cha uzimu. Koma pali malire pa zimene Mulungu amachitira mkhristu m'moyo uno. Musayembekezere moyo wodzazidwa ndi Mzimu komanso moyo woyeretsedwa kukhala oposera zimene Mulungu analonjeza. Pali zinthu zina zimene sinasungidwira kumwamba.

1. Werengani Aroma 8:2, 18-27.
   a. Kodi Mzimu anamuchitira chiyani Paulo, kolingani ndi 8:2?
   b. Kodi nyengo za dziko tsopano lino ziri bwanji kwa a Khristu?
      (1) vesi 18
      (2) vesi 20
      (3) vesi 22
   c. Ngakhale kuti Mzimu amatimasula kuchoka ku lamulo la uchimo ndi ifa, timakhalabe mu dziko la mavuto. Kodi Mzimu adzatichitira chiyani kwa ife pakati kati pa mayesero? (Aroma 8:26)
2. Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chifooko motani m'moyo wa Paulo (2 Akorinto)
3. Ngakhale kuti Khristu anali omvera Mulungu kwa thunthu ndi opanda chimo (1 Petro 2:21-22), anakhalabe ndi malire, zovuta, kudedwa komanso masautso ngati mbali imodzi yakukhala ndi moyo ngati munthu. Kodi zina mwa izo ndi chiyani?
   a. Mateyu 13:57
   b. Mateyu 26:38-40
   c. Luka 4:1-2
   d. Luka 19:45
   e. Yohane 11:35
   f. Kodi ndi chiyani chimene munakumana nacho chimene chinali chovuta komabe munakakamira kukhalabe ngati Khristu?
4. Werengani Ahebri 4:15.
   a. Kodi Yesu anayesedwa m'njira zotani?
   b. Kodi kuyankhapo kwake kunali kotani?
   c. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa yesero ndi chimo?
5. Kodi ndi lonjezo lotani limene Mulungu amapanga kwa inu pamene mukuyesedwa? (1 Akorinto 10:13)
6. Kodi m'Khristu angasiyanitse motani pakati pa chabwino ndi choipa?
   a. 1 Yohane 2:6
   b. Aefeso 5:10

7. Machitidwe anthu ku maimvaimva monga mantha akhoza kukhala a uchimo kapena a umunthu. Werengani malo awiri pamene Petro anachita mantha. Kodi ndi machitidwe oti amene anali a uchimo ndipo ndi machitidwe oti amene anali a umunthu. Chifukwa chiyani? (Marko 14:66-71 komanso Machitidwe 4:29-31)

8. Kodi moyo wa uzimu wa Paulo unali otani? (Machitidwe 13:9)

   Kodi ndi sautso kapena vuto lotani limene anakumana nalo pa Aefeso 6:12?

   Pa 2 Akorinto 11:28?

   Kodi ndi masautso kapena zipsinjo zotani zimene mwaona anthu odzazidwa ndi Mzimu amakumana nazo?

9. Kodi Yesu analamula chiyani kwa ophunzira ake pa Mateyu 5:48?

   Kulingana ndi Mateyu 5: 43-47, kodi ndi mbali iti kapena gawo iti la moyo wanu limene liyenera kukhala "bwino" ("bwino" akutanthauza kugwiritsa ntchito bwino cholinga chimene chinthu chinapangidwira.)

   Kodi kutsindika kwa chikondi uku kukuonetsedwa motani mu Mateyu 22:37-40?

   Kodi njira yabwino yochotsera mantha a chiweruzo ndi iti? (1 Yohane 4:17-18)

   Kodi chikondi chimachokera kuti? (Agalatiya 5:22)

   Kodi chikondi chimachita chiyani? (Aroma 13:9-10)

10. Pamene mwadzazidwa ndi Mzimu ndi kupangiwa kukhala woyera, kodi ndi chiyani chimene Mulungu amayembekezera kwa inu?

    a. Akolose 1:22-23

    b. Agalatiya 5:25

    c. Afilipi 4:8

11. Kodi kufunikira kwa kusautsidwa, mayesero kapena chizunzo kwa m'khristu ndi chiyani? (Aroma 5:3-5)

12. Kodi tikuyembekezera chiyani kumwamba (1 Yohane 3:2)

    Kodi tikuchita chiyani pano komanso tsopano lino kukonzekera nthawi imeneyo? (1 Yohane 3:3)

13. Kodi ndi mavuto oti amene adzachotsedwa ndi kumwamba? (Chivumbulutso 21:4)

    Kodi izi zalonjezedwa kwa ndani? (chivumbulutso 21:7)

14. Mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu adzakumanabe ndi mavuto, komanso nkhondo. Limodzi mwa mabuku a chikhristu limene liri ndi chilimbikitso cha mphamvu mu dziko ndi, *The Christian's Secret of a Happy Life*, lolembedwa ndi Hannah Whitall Smith. Adapeza chimene zimatanthauza pakunena kuti nkhondo ndi ya Yehova:

    > Ndinatembenuka mu chaka cha 1856, apo dili ndi zaka 26 za kubadwa. Patapita nthawi Ambuye mwa chisomo ananditsogolera mu chidziwitso cha choonadi chochuluka. Koma mtima wanga siunali m'malo mwake. Pakutha pa zaka zisanu ndi zitatu za moyo wanga wa chikhristu ndinakakamizidwa kuvomereza mwa chisoni kuti ndinalibe mphamvu zambiri zogonjetsera chimo ngati mmene ndinalili pamene ndinatembenuka kumene.
    >
    > Ndinayamba kufunafuna chiyero. Ndinayamba kubuula pansi pa goli la uchimo umene ndinali womangidwa nawo. Koma ndinali otsimikizika mtima kwa thunthu kuti mphamvu, maganizo

kapena mapemphero anga sakwanira, ndipo sindinali kuzindikira njira ina ili yonse, ndipo ndinali pafupifupi okonzeka kusiya opanda chiyembekezo.

Mu nthawi imeneyi ya chosowa (1863) Mulungu anandibweretsera ena amene chidziwitso chawo chinaoneka chosiyana ndi changa. “Anatsimikiza” kuti apeza “njira ya chiyero” mmene moyo opulumutsidwa ukhoza kukhala komanso kuyenda mu mtendere okhazikika, ndipo ukhoza kupangidwa “kukhala oposa a gonjetsi” kudzera mwa Ambuye Yesu Khristu.

Ndinawafunsa chisinsi chawo ndipo anayankha, “Mwachidule ndi kusiya macitidwe athu ndi kudalira Mulungu kuti atipange kukhala woyera.”

Sindidzaiwala kudabwa kumene yankho ili linandipatsa… .

Ngati vumbulutso la ulemero wa kuthekera kwa moyo otero unafika pa ine, koma mfundoyi inali ya chilendo kwa ine, kuti ndiigwire. Ndinali operewera m’maganizo mwanga pakuyerekezera kukhala kwa tsiku ndi tsiku. Ndinali ndisanalotepo kudalira Ambuye pa zimenezo, ndipo sindinadziwe kuchita kwake… . Ndinayamba kusanthula malemba kwa kwatsopano. Ndinapeza kuti pondifera, anadipatsa chipulumutso changwiro… . Ndinapeza kuti anadzipereka kwa ine ngati moyo wanga, ndipo kuti anafuna kubwera mu mtima mwanga ndikutenga ulamuliro wa zonse mmenemo ndikudzitengera yekha zinthu zonse. Anadziwonetsera kwa ine wangwiro komanso wa thunthu komanso Mpulumutsi wopezekeratu, ndipo ndinapereka zanga zonse kwa Iye, ndinadzikhuthula, ngati kuti ndikulowa, mu nyanja ya chikondi chake, kuti zinthu zitheke mwa ine kudzera mu ntchito yake ya mphamvu. Ndinakhulupirira choonadi chakuti anali chiyeretso komanso chilungamitso, ndipo moyo wanga unapeza mpumulo pambuyo pake, mpumulo wakuti mawu sangafotokonzere — mpumulo pa masautso a kumva kuperewera, mpumumulo ku nkhondo zonse zowawa, mpumulo ku zolephera zonse. Chisinsi cha chiyero chinaonetsedwa kwa ine, ndipo chisinsi chimenecho chinali Khristu. Moyo wanga walowa mu mkati mwa kupumula kapena “kusunga sabata” kumene mtumwi Paulo akunena pa Ahebri 4:9, “kotero tsono kwatsala mpumulo wa tsiku la Sabata kwa anthu a Mulungu.” Osati kuti palibe makangano; koma nkondo siyanganso, koma ya Khristu.

Nthawi yonse yakale ya maphunziro anga ikuoneka idali yotaika. Nthawi yonse yakumbuyo ya umoyo wanga wa chikhristu ndikalinganiza, inaoneka yotayika. Ndizoonadi ndinali mwana wa Mulungu, koma kukula kwanga kunali kokwinimbira, ndipo machitidwe anga anali ofooka. Pamene chisinsi ichi cha chikhulupiliro chinaululidwa kwa ine, ndinayamba kukula; ndipo kudzipereka kumene kunali kosatheka kwa ine kunasanduka chimwemwe cha mtima wanga.

Kukhulupirira, kupumula, kukhazikika — izi ndi mbali yanga; Iye amachita zina zonse. Kutalika kwa chikondi, kuzama kwa chikondi, chisamaliro chopambana, kukonda kwa nzeru kwa mwambo, kusunga kopambana, kudabwitsa kwa kuulula, mphamvu mchifooko; chitonthozo cha pa chisoni, kuwala mu mdima mu kuthetsa kwa mavuto kumene ndinakupeza; Mulungu wodabwitsa, ndi mpulumutsi wodabwitsanso; palibe mawu amene angafotokozere! (J. Sidlow Baxter, *His Deeper Work in Us*, Grand Rapids: Zondervan Publishing House, 1967.) 81-82.

15. Santhulani moyo wanu wa uzimu.

   a. Kodi ndi mavuto oti a moyo wanu amene simuyembekezera kuti Mulungu kuwachotsa m’moyo uno?

   b. Kodi ndi mbali iti imene mukufunika chilangizo?

   c. Kodi ndi dera liti limene mungayembekezere Mulungu kukupatsani chigonjetso?

d. Kodi ganizo lanu lotsatira limene likufunikira kuti mukumane ndi chigonjetso chimenecho ndi iti?

Mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera akhoza kukumana nazo m'moyo. Ngakhale kuti Mulungu sachotsa mavuto onse, pali njira zina za mphamvu zimene Mulungu adzachita kudzera m'moyo mwanu. Zina mwa izo zakambidwa mu phunziro lotsatira.

## Vesi Loloweza

Koma anandiuza kuti, "chisomo changa ndi chokwanira pakuti mphamvu zanga zimaoneka kwathunthu mwa munthu wofowoka." Choncho ndidzadzitamandira mokondwera chifukwa cha zofowoka zanga, kuti m'kutero mphamvu ya Khristu ikhale pa ine (2 Akorinto 12:9).

# Phunziro 8 la Baibulo

# Zimene Mzimu Woyera adzachite kudzera mwa inu

Pali zabwino zambiri zimene Mzimu Woyera angabweretse komanso adzabweretsa m'moyo mwanu ngati mutapempha. Mukuyenerabe kukhala mu dziko lodzadza ndi mavuto – koma Mzimu Woyera yemweyo amene amabweretsa mtendere ndi chiyero ku mtima wanu adzabweretsa madalitso kudzera mwa inu mu njira za mphamvu.

1. Onani pa zitsanzo izi pa oyera mtima ena mu buku la Machitidwe. Onetsani chimene Mzimu anachita mwa iwo—ndi kudzera mwa iwo.

   a. Mwa Petro (Machitidwe 4:8)

   Kudzera mwa Petro (Machitidwe 4:9-12)

   b. Mwa Stefano (Machidwe 7:55)

   Kudzera mwa Stefano (Mchitidwe 7:59-60)

   c. Mwa Barnaba (Machitidwe 11:24)

   Kudzera mwa Barnaba (Machitidwe 11:24)

   d. Mwa Paulo (Machitidwe 13:9)

   Kudzera mwa Paulo (Machitidwe 13:10-12)

2. Tiyeni tionepo mwapadera pa nkhani ya Filipo, amene akhoza kufotokozeredwa ngati mmodzi mwa wosankhidwa pakati pa anthu mu mpingo woyamba.

   a. Molunjiika, kodi udindo wa Filipo mu mpingo unali otani? (Machitidwe 6:1-5)

   b. Kodi ndi kwa ndani kumene anachitira umboni ndi chifukwa chiyani umboni unali ofunikira? (Machitidwe 8:26-27)

   c. Kodi mulingo wa tcheru wa Filipo kwa Mzimu Woyera unali otani? (Machitidwe 8: 29-30)

   d. Kodi chisinsi cha mphamvu ya Filipo komanso kuthekera kwake kunali chiyani? (Machitidwe 6:3 ndi 5)

3. Pamene Khristu anadzipereka yekha "kutiwombola ku zoyipa zonse ndi kudziyeretsera yekha anthu amene ndi akeake," kodi cholinga chake ndi chiyani pa anthu ake omwewa chimene chidzakhuda dziko lowazungulira? (Tito 2:14)

4. Kodi zochitika za iwo amene anali wofuna zinali chiyani ngati zotsatira za kukhudzika kwa ophunzira odzazidwa ndi Mzimu Woyera pa Machitidwe 4:31-35?

5. Fotokozani nthawi imene munawona mkhristu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera akuchitapo kanthu pa chosowa.

6. Mphamvu ya kukonda ndi kupeza chimwemwe pa vuto imaonekera mu miyoyo ya okhulupirira monga Stefano pa Machitidwe 7:55-60 komanso Paulo ndi Sila pa Machitidwe 16:25. Kodi ndi chiyani kapena ndi ndani amene ndi chiyambi cha zinthu monga chikondi ndi chimwemwe? (Agalatiya 5:22)

7. Kodi Mulungu amafuna kuti mumutumikire motani? (Luka 1:74-75)

8. Ganizirani anthu wamba kuchita china cha padera kwa Mulungu.

   a. Kodi anthu amatenga kuti kuthekera kwa kuchita ma utumiki a padera kwa Mulungu? (1 Akorinto 12:4-6)

   b. Kodi ndi chiyani chimene chiyenera kulamulira kagwiritsidwe ntchito ka mphatso ina iliyonse? (1 Akorinto 12:7)

   c. Werengani mndandanda wa mphatso, kuthekera, komanso chisomo mu ndime zotsatira ndipo lembani mphatso imodzi kuchokera pa mndandanda uli wonse.

      (1) 1 Akorinto 12:8-11

      (2) Aroma 12:6-8

      (3) Aefeso 4 :11-12

      (4) Petro 4:9-11

   d. Kodi ndi mphatso yanji (zanji) zimene mukuganiza kuti Mulungu wakupatsani, ndipo muigwiritsa (muzigwiritsa) ntchito motani kuti mukwaniritse zosowa za mtsogolo?

9. Kodi Mulungu amakupatsani mphamvu yake kuti? (Aefeso 3:16)

10. Kodi Paulo anadziwa motani mmene ayenera kuchitira utumiki wake? (Machitidwe 13:2 ndi 16:7)

11. Kodi ndi ntchito iti imene ikuoneka yosatheka imene Khristu anapereka kwa ophunzira ake? (Mateyu 28:19-20 ndi Luka 24:46-48)

   a. Kodi ndi chosowa chotani chimene anali nacho ngati akanati akwaniritse ntchito iyi? (Luka 24:49)

   b. Kodi chosowachi chikanakwaniritsidwa motani? (Machitidwe 1:8)

   c. Kodi chokwaniritsa cha Mulungu cha lonjezo iri chinali chiyani pa Machitidwe 1:8? (Machitidwe 2:4-12)

   d. Petro pamodzi ndi ophunzira anali odzaza ndi Mzimu Woyera. Kodi zotsatira zake pa Machitidwe 2:41 pamene analalikira ndi kuchitira umboni zinali chiyani?

   e. Fotokozani za nthawi imene Mzimu Woyera anakuthandizani kuchitira umboni.

12. Kodi chilipo chimene chikutchinga mphamvu ya Mulungu m'moyo mwanu?

13. Samuel Logan Brengle anali wamkulu mu Salvation Army. Mabuku ake oposa wanu miliyoni adalitsa dziko. Tiyeni tiona gawo la nkhani yake:

> Pa 9 January 1885, cha mu ola la chisanu ndi chinayi, Mulungu anayeretsa mtima wanga. Ndinali mu chipinda changa pa nthawi imeneyo, koma mu mphindi zochepa ndinatuluka kukakumana ndi munthu ndi kumuuza zimene Mulungu wandichitira. Mmawa mwake ndinakumana ndi bwenzi lina pa msewu ndikumuuza nkhani yodala. Anakuwa ndi kuyamika Mulungu ndi kundilimbikitsa kulalikira uthenga ndi kuwuvomereza pali ponse. Mulungu anamugwiritsa ntchito kundilimbikitsa ndi kundithandiza. Motero tsiku lotsatira ndinalalikira pa uthenga momveka bwino komanso mwa mphamvu mmene ndikanathera, ndipo ndinamaliza ndi umboni wanga.
>
> Mulungu anadalitsa mawu ake mwa mphamvu kwa ena, koma ndikuganiza kuti anawadalitsa kwambiri kwa ine. Kuvomereza kumeneko kunandiika pa mbiri. Kunadula malire. Maiko

atatu tsopano anali kuwona ine ngati mmodzi amene anaonekera amene Mulungu anamupatsa mtima wabwino. Sindinabwererenso m'mbuyo. Ndinayenera kupitabe patsogolo. Mulungu anawona kuti ndinayenera kukhala owona kufikira imfa. Choncho patapita masiku awiri, m'mawa, nditangodzuka kumene pa kama ndipo ndinali kuwerenga ena mwa mawu a Yesu, anandipatsa mdalitso wakuti sindinalotepo kuti munthu akhoza kukhala nawo ku mbali ino ya kumwamba. Kunali kumwamba kwa chikondi kumene kunabwera mu mtima mwanga. Ndinayenda kutuluka kupita ku Boston Common ndisanadye chakudya cha mmawa kulilira chimwemwe komanso kuyamika Mulungu. Oh, mmene ndinazikondera! Mu ola limenelo ndinamdziwa Yesu ndipo ndinamukonda moti mtima wanga ukanasweka ndi chikondi. Ndinakonda mbalame za machacha, ndinakonda agalu, ndinakonda a kavalo, ndinakonda ana a umphawi m'misewu, ndinakonda alendo amene anandidutsa, ndinakonda anthu a chikunja —ndinakonda dziko lonse.

Kodi mukufuna kudziwa kuti chiyero ndi chiyani? Ndi chikondi cha ngwiro. Kodi mukufuna kudziwa kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chiyani?  Si chinthu choseweretsa. Sichinthu chongofuna kusangalatsa chimene chimangobwera mwa usiku umodzi. Ndi ubatizo wa chikondi umene maganizo onse amalunjika kwa Yesu [2 Akorinto 10:5]; umene umachotsa mantha onse (1 Yohane 4:18); umene umapsereza chikaiko komanso kusakhulupirira monga ngati mmene moto umapserezera' umene umapangitsa wina wake kukhala "wofatsa ndi wodzichepetsa." (Mateyu 11:29); umene umapangitsa wina wake kudana ndi chidetso, kunama komanso chinyengo, lilime labodza komanso njira ina iliyonse yodana ndi udani waukulu; zimene zionetsa Kumwamba ndi Gehena; zemene zipangitsa wina kukhala woleza mtima ndi wina wofatsa ndi zinthu zovutitsitsa komanso chimo; umene umapangitsa wina kukhala "wangwiro, … wa mtendere, … kukhala woganizira za ena, wogonjera, wodzala ndi chifundo komanso zipatso zabwino, osakondera ndiponso woona mtima" (Yakobo 3:17); umene umabweretsa wina wake mu mchiyanjano chosatha ndi Ambuye Yesu molimbikira kuyesetsa kuti abweretse dziko lotaika ndi lochimwa kwa Mulungu.

Mulungu anandichitira zonsezi, lidalitsike dzina lake loyera! (Samuel Brengle, *Helps to Holiness*, London: Salvationist Publishing and Supplies, Ltd., 1955.)

14. Ganizirani pang'ono! Kodi mukuganiza kuti Mzimu Woyera akhoza kuchita chiyani kudzera mwa inu?

Mukhoza kudzazidwa ndi Mzimu ndi kuyeretsedwa kwa thunthu. Kodi munadzazidwa? Mukhoza kukhala komanso kuyenda ndi Mzimu ngati chinthu cha nthawi–ndi-nthawi. Kodi mukutero? Mzimu Woyera adzachita zazikulu kudzera mwa inu. Kodi akuchita? O Ambuye, kwa masiku anga a mtsogolo, ndikufuna kukumana ndi kukula kwa ulamulro wanu m'moyo mwanga.

## Vesi Loloweza

Choncho iye anandiuza kuti, "Mawu a Yehova kwa Zerubabeli ndi awa: 'Osati mwa nkhondo kapena ndi mphamvu, koma ndi Mzimu wanga,' akutero Yehoha wa mphamvu zonse" (Zekariya 4:6).